Yekha, ndiponso Muhammad ndi Mneneri Wake.

Mau awa ayenera kucokera pansi pamtima ndiponso atsimikizidwe ndi nchito zathu. Mukuikira umboni umenewu, munthu ali kukanilatu milungu ina yonse yaboza, ndiponso ali kutsimikiza kuti Allah cabe ndiye Yekha ofunika kumugwadira ndiponso iye avomera kuti Mtumiki Muhammad (Mtendere Ukhale Kwa Iye) ndi Mtumiki wa Allah wosiliza. Kutero kumapanga munthu khala Msilamu.

## 2. Mapemphero Asanu pa Tsiku

Mapemphero amakhadzikitsa ubale wanyama ndi wauzimu pakati pa munthu ndi Mlengi wake, ndiponso ndi cikumbutso ca nthawi zonse kwa munthu pazimene afunika kucita mogonjela malamulo a Mulungu.

Mapemphero asanu patsiku anakhadzikitsidwa kamodzi mmbandakucha, masana, masana dzuwa litapendeka, pamene dzuwa lilikulowa, ndiponso pamene usiku ulinkungena.

Kupemphera pemphero lili lonse kumatenga kanthawi kocepekera ndithu, mmene opemphera amawerenga mau ocokera mu Quraan, kupempha ndi kuthokoza Allah, ndiponso kusintha moimirira, moweramira mogwadira ndizina zotere. Pokonzekera pemphero, Msilamu amasamba ziwalo zina zathupi monga manja, kumaso, mmutu, mmendo kuti iye akwaniritse kuziyeletsa thupi ndi mzimu wake.

## 3. Copeleka ca Pacaka

Kupeleka copeleka ca pacaka ndikokakamizidwa kwa Msilamu aliyense amene ali ndi cuma cokwanira kuti angathe kucotsa copeleka. (Mwacitsanzo iye ayenera kukhala ndi cuma copitilira muyeso umene unakhazikitsidwa).

Msilamu wacuma ayenera kucotsa zigawo ziwili ndi theka za cuma cake ca pacaka ndikupeleka kwa anthu ofunikira kuwapatsa monga osauka, ali mmavuto ndiponso amene ali ndi nkhongole. Copereka ici cimayeretsa cuma ca Msilamu ndipo ciri ndi phindu zoculuka kwa onse opereka ndiwolandira. Phindu lina limodzi ndilakuti copereka ici cimacepetsa mpata umene umakhala pakati pa olemera ndi osauka, kotero kuti aliyense amapeza zofunikira zaumoyo.

## 4. Kumanga (kapena kusala kudya ndi kumwa) kwa pa Caka

Caka ciri conse, mumwezi wa Ramadhan, Asilamu amamanga kucokera mmbandakucha kufikira dzuwa litalowa. Iwo amakhala patali ndi zakudya, zakumwa ndiponso nchito yolemekeza ukwati mmbanja.

Kumanga kumathandiza munthu munjira yoziyeretsa muuzimu, kumaphunzitsa munthu kukhala wopilira ndikuzigwira ndiponso kuli ndi phindu za thanzi lathu zambili.

Ramadhan ndimwezi wa cisanu ndizinai mu "calendar" ya Cisilamu.

## 5. Ulendo wopita ku Makkah.

Ulendo wopita kuMzinda Woyera wa Makkah, mu dziko la Saudi Arabia, uyenera kupangidwa kamodzi paumoyo wa Msilamu ali yense amene angathe kutero, ngati alinaco cuma ndi thanzi.

Uledowu (wocedwa Hajj) umapangidwa caka ciri onse mumwezi wa khumi ndiziwili, kugwirizanitsa anthu amitundu yosiyana-siyana, maonekedwe ndi zaka ndiponso zilankhulidwe zosayana-siyana, pamene onse amakumana pamalo amodzi kugwadira Mulungu Mmodzi Wacoonadi. Ulendu waukulu ndiponso wolemekezeka uwu uli ndi zigawo zambiri zo phatikiza kupereka nsembe, kuyenda ndikumapemphera mmalo osiyana-siyana. Ulendo uwu umakwanitsa kusintha moyo wa munthu ndikumupatsa kuzicepetsa ndiponso kumupatsa kupilira ndikuthokoza.

Anthu onse amene amapita pa Ulendo uwu amabvala zobvala zolingana komanso zamutengo wapansi. Izi zimathandiza kucotsa kusiyana kumene kumakhala pakati pa anthu ndikuzakhala anthu amodzi pamaso a Mulungu.

## Kugwadira Mulungu

### Ncito ili yonse imene imasangalatsa Allah.

Mu Mpingo wa Cisilamu, kugwadira Mulungu sikuli mu nsandamira zisanu cabe, ai. Kugwadira Mulungu kutanthauza kugwira nchito zonse zimene zingathe kumusangalatsa Mulungu. Nchito zonse zabwino zikhoza kukhala njila yomugwadiliramo Allah, pokapo ngati ife tayeretsa colinga cathu ndiponso poona kuti nchitozo zili zogwilizana ndi malamulo a Mulungu. Zitsanzo ndi izi: kunyemwelera, kukhala wabwino kwa ophatikizana naye,. Kuthandiza banja lako, kukhala wokhulupilirika ngakhale kucotsa zinthu zimene zili zonyantsa kapena zingapweteke anthu panjira.

Tifunika kuzindikira kuti Allaah saamalabadira nchito zathu zabwino, ai. Koma ife ndife amene timufuna Allaah, ndiponso nchito zonse zabwino zimene ife timagwira zimatiphindulira ife eni.

## Mapeto

Mau acikhulupiliro ndiponso nchito zabwino zimene zaculidwa pamwambapa ndiye zimene zimamanga Mpingo wa Islam.

Ngati tautsata bwino Mpingo wa Islam, umakwaniritsa ndukipatsa zonse zimene zili zofunikira kwaife muuzimu, muthupi, munzelu ndiponso zifunilo zonse za anthu onse. Mpingowu ndinjira yaumoyo yosavuta kuitsatira, ndiponso yowongoka. Ndiyo njira imodzi yokha imene Ambuye Mulungu anaivomela ndiponso ndiyo cabe njira imene ingatipeleke ku cikondwelero cosatha mu Malo aMtendere (Paradise).

**"Aliyense amene amagwira nchito zabwino, mamuna kapena mkazi, pamene iye ali okhulupilira – ndithudi Ife Tizacita kuti iye ahkale ndi umoyo wabwino, ndiponso ndithudi Ife Tizawapatsa malipiro awo (mokwana ku umoyo umene uli kubwela wa Kumwamba), malingana ndi ubwino wazinchito zawo zimene iwo anali kugwira."**
Quraan 16:97.

**Ngati tifuna kuziwa zina zambili ndiponso ma "Pamphlets" ena :**

**www. islamic-invitation.com**
**www. islamicpamphlets.com**

# Za Mpingo wa Islaam

## Mau acidule

## Phunzilani za zofunikira mwacidule



التعريف بالإسلام باللغة النيانجا

www.islamic-invitation.com

## Za Mpingo wa Islam

Islam ndi njila ndiponso mkhalidwe wa umoyo wokwanira. Islam imamulimbikitsa munthu kuti aikile nzelu ku ubale wake ndi Mlengi (Mulungu) wake. Mpingo wa Islam umaphunzitsa kuti munthu atha kupeza cikondwelelo cosatha ndiponso mtendere wosatha kupyolera mukukhala kwake pafupi ndi Mulungu, potsatila malamulo a Mulungu ndiponso pogwila nchito zabwino.

Ciwelengelo ca Asilamu padziko lino lapansi lero cili cigawo cimodzi muzigawo zisanu za anthu onse padziko lino lapansi. Izi zitanthauza kuti Mpingo wa Islam ndi mmodzi wa mipingo yaikulu mudziko lino lapansi. Kukulupilira ndi kugwadira Mulungu Mmodzi yekha wa Coonadi, ndiye colinga ca umoyo uno, ndiponso uyu ndiwo musana wa Mpingo wa Islam.

Liu la ci Arabu loti "Islam" litanthauza kuti kugonjera ndiponso kuzipeleka kwa Mulungu Mmodzi yekha wa Coonadi. Munthu ali yense amene amagonjera mwa Mulungu Mmodzi yekha, iyeyo acedwa kuti Msilamu, ndiponso akoza kukhala wa mtundu uli wonse ndiponso wa makhalidwe kapena maonokedwe ali onse.

Mpingo wa Islam ndiwosiyana ndi Mipingo ina yonse cifukwa cakuti Mpingowu siutenga dzina lace kucokera ku dzina la munthu kapena mtundu.

## Nsandamila 6 za Cikhulupiliro

### 1. Kukhulupilira mwa Allah.

Allah ndilo dzina la Mulungu Mmodzi Woona.

"Allah" ndilo dzina la Mulungu Mmodzi Woona mu cilankhulidwe ca ci Arab. Iye Allah alibe adani, alibe othandizana naye, alibe olingana naye, alibe ana kapena makolo. Iye saali ngati zolengedwa zake cifukwa kulibe cilengedwe cili conse cimene cilingana Naye. Ena mwa maina ndi mphamvu zake ndiaya: Mlengi, Wacisoni, Wapamwamba-mwamba, Wa Mphamvu Zonse, Wolungama, Wanzelu, Wosamala ndiponso Wodziwa Zonse.

Iye ndiye Mlengi ndiponso Msamali wa zonse, Amene anatipatsa ife madalitso osawelengeka, monga madalitso a kumva, kuyangana, kuganiza ndiponso madalitso okwanisa kuyenda, kulankhula ndiponso kukwanisa kupanga zinthu. Cifukwa ca ici ife tifunika kubvomela ndiponso kumuthokoza ndi kumugwadira iye Yekha ndi kutsatila ciwongoko Cake.

Tikayanganisisa kalengedwe ka dziko lino lapansi ndiponso mwamene liyendera ndicoonekelatu kuti dzikoli linapangidwa ndi Wanzelu ndiponso wa Mphamvu. Conco ndimaganizo opanda pace kuganizila kuti dziko lino linadzipanga lokha kapena linapangidwa ndi zina zocitika.

### 2. Kukhulupilira mwa Angelo

Angelo ndizilengedwe za Allah zimene zinalengedwa kucokera mukuwala, ndiponso zinapatsidwa nchito zocita ndiponso sizinyozela malamulo a Allah. Mbili za Angelo ena ocepekela zinabvumbulutsidwa monga Mngelo Gabriele, amene ankabweletsa uthenga wa Allaah kwa Aneneri, ndiponso Mngelo wa imfa amene amatenga mizimu ya anthu panthawi ya imfa.

### 3. Kukhulupilira mu Mabhuku obvumbulutsidwa

Allah anatumiza uthenga wa cibvumbulutso kwa Atumiki Ake monga ciongolo ndi cifundo Cake kwa anthu. Uthengawu unali ma Bhuku monga TORAH limene linabvumbulutsidwa kwa Mtumiki Mose, ndi Mbili ya Bwino (GOSPEL) limene linabvumbulutsidwa kwa Mtumiki Yesu Kristu, ndiponso QURAAN limene linabvumbulutsidwa kwa Mtumiki Muhammad (Mtendere wa Mulungu Ukhale Kwaiwo Wonse).

Quraan ndi Mau a Mulungu ndiponso cibvumbulutso ca Mulungu comaliza kwa anthu onse. Mu Quraan muli zizindikilo zili poyera komanso zodabwitsa zimene zisonyeza kuti ndithu Bhukuli licokera kwa Mulungu. Zina mwaizi ndiizi:

· Muli uthenga wabwino wa dziko lonse lapansi wosavuta kumvetsetsa ndiponso wogwilizana ndi maganizo ndi cikhulupililo ca anthu kwa Mulungu wa Mphamvu.

· Muli cilankhulidwe cabwino codziwika padziko lino lonse malingana ndi cilankhulidwe cokongola ca ci Arab – komanso Quraan imeneyi inabvumbulutsidwa kwa Mtumiki Muhammad (Mtendere Ukhale Kwa Iye) yemwe ndicodziwika mu mbili ya anthu kuti iye analibe maphunzilo adziko lino.

· Muli umboni wogwilizana ndi kutsimikiza za maphunziro a Science zimene zina ululidwa posacedwapa, ngakhale izo zinabvumbulitsidwa zaka 1,400 zapita.

· Mau amu Quraan anasungidwa modabwitsa, liu ndi liu mucilankhulidwe ca Arabic, kucokera nthawi imene Bhukuli linabvumbulutsidwa – mosiyana ndi ma Bhuku ena a Mulungu amene anaonongedwa kapena kusinthidwa kapena kusowelatu kumene.

Cidabwitso cina ca Quraan ndicakuti mkati mwa Bhukuli mulibe mau olakwika kapena mau otsutsana.

Kulibenso kumasula kwina kwamene tingamasule poganizila za zodabwitsa zili mu Quraan, koma cabe kubvomera kuti Bhukuli linacokera kwa a Mbuye Mulungu. Mogwilizana ndi miyambo ndi mau a Mtumiki Muhammad (Mtendere Ukhale Kwa Iye), Bhukuli ndilo nkhokwe ya ziphunziso za Cisilamu.

### 4. Kukulupilira mwa Atumiki

Asilamu amakhulupilira kuti Allah anatumiza zikwi ndi zikwi za Atumiki, ku maiko ndi mitundu yonse ya anthu, kuti afikitse uthenga wa Mulungu. Mkati mwa Atumiki awa munali: Adam, Noah, Abraham, Davide, Yosefe, Mose, Yesu Kristu ndi Muhammad (Mtendere wa Mulungu Ukhale Paiwo Wonse). Nchito yawo inali yobweza anthu kuti amgwadire Mulungu Mmodzi Yekha, kukhala monga zitsanzo kwa anthu pomugwadira Mulungu ndiponso kuwatsogolera anthu kunjila ya cipulumutso. Atumiki awa alibe mbali ina ili yonse mu Mphamvu za Mulungu, ndiponso mapemphero onse amene anthu amapempha thandizo kucokera kwa Atumiki kapena kupemha kwa Mulungu kupyolera mwa Atumiki, ndizoletsedwa ndiponso ndikunyozera Mphamvu ya Mulungu yakuti anthu azimugwadira Iye yekha.

#### - Mtumiki Yesu

Asilamu amakhulupilira kuti Yesu Kristu ndi Mtumiki wolemekezeka wa Mulungu amene anabadwa modabwitsa mwa amai ake Mariya. Iye anaonesa zodabwitsa zambiri kupyolera mu Mphamvu za Mulungu monga kucilitsa odwala, kucilitsa odwala khungu ndiponso kulankhula kwake kwa anthu ali mwana wa tsiku limodzi lobadwa, moimilira amai ake amene anali kunyozedwa ndi anthu. Ngakhale Asilamu amamulemekeza ndiponso kumukonda Yesu, iwo saamamugwadira iye ngati Mulungu. Asilamu saamamutenga Yesu monga Mwana wa Mulungu ai, ndiponso iwo saamakhulupilira kuti Yesu ndimmodzi wa atatu mu Mphamvu za Mulungu kapena kukhulupilira kuti iye (Yesu) ali nazo zina mwa Mphamvu za Mulungu mwa iye.

Mulungu akuti: **"Sicili cotheka kuti Allah akhale ndi mwana wacimuna; Iye ndiwolemekezeka! Iye akafuna kulenga cinthu amangoti 'Cicitike' ndiponso cimacitika".** Quraan: 19:35

#### - Mtumiki Muhammad

Muhammad (Mtendere Ukhale Paiye) anali Mtumiki wosiliza wa Allah kwa anthu onse. Iye anabwela ndi Quraan kudzaonesa anthu mwamene angatsatile ziphunziso zimene zili mkati mwace, ndiponso iye anali citsanzo cabwino ca munthu okhulupilirika, wacilungamo, wacifundo, womvetsetsa, wokamba coonadi ndiponso olimba mtima. Cimozi mozi monga Yesu Kristu, Asilamu saamamugwadira Muhammad monga Mulungu, ai.

### Kukhulupilira mu Tsiku Laciweruzo

Tsiku la Ciweruzo nditsiku loopsya limene aliyense waife anthu azafunika kuti akaimilile pa Maso a Mlengi wathu ndikuyankha mafunso okhudzana ndi nchito zathu zabwino kapena zoipa. Nchito ili yonse imene ife tinagwira pano padziko lapansi, yain'gono kapena yaikulu, tizafunsidwa paTsikuli.

Pa Tsiku loopsyali, Allah, Mfumu ya Cilungamo, azaweruza ndikukhadzikitsa milandu zonse za anthu, niponso palibe munthu ngakhale mmodzi amene adzadandaula ndi ciweruzo ca Allah. Zofunikira za munthu ndi munthu zizapatsidwa kwa ene ace. Anthu onse azaweruzidwa mwacilungamo ndiponso ali yense azalipilidwa malipiro ake amene adzakhala mwina Malo a Mtendere kapena cilango mu Moto waku Gehena.

Popanda Tsiku la Ciweruzo, umoyo wa pano padziko lapansi siungakhale bwino, cifukwa sialiyense wa ife amene amalandira cilungamo pano padziko la pansi.

### Kukhulupilira mu Zocitika mu Mphamvu za Mulungu

Allah amadziwa zonse zimene zinaticitikira mmbuyo, zimene ziticitikira pakali pano ndiponso zimene zizaticitikira mtsogolo. Iye ali ndi Mphamvu pa zinthu zonse – palibe ciri conse cimene cingacitike popanda Nzelu Zake ndiponso Cilolezo Cake.

Munthu aliyense anapatsidwa ufulu wosankha pakati pa Cabwino ndi Coipa ndiponso iye azafunsidwa molingana.

Kukhala ndi ufulu wosankha sizitsutsana ndi coonadi cakuti zinthu zimacitika mu Nzelu ndi Cilolezo ca Mulungu. Kapena kuti izi zimatanthauza kuti Mphamvu za Mulungu pa zinthu zonse zimaletsa anthu kukhala ndi ufulu wosankha, ai. Nzelu za Mulungu pali zimene anthu amasankha kucita sizitanthauza kuti anthu ali okakamizidwa kucita zinthuzo, ai, ndiponso Ambuye Mulungu sikuti amakhala okondweletsedwa ndi zonzse zimene Iwo amalola kuti zicitike.

## Nsandamila 5 za Cipembezo

### Ciyambi ca umoyo wa Msilamu

### 1. Kuikira Umboni wa Cikhulupiliro

BKuikira umboni wa Cikhulupiliro ndi kukamba mau awa: Palibenso wina wompembedza mwacoonadi koma Mulungu